KATEKISIMU WA ANA AANG'ONO KWAMBIRI

KUDZIWITSA KOYAMBA ZA CHIPHUNZITSO CHA BUKU LOPATULIKA

Loyenera ana a ang'ono a chipangano

Lalembedwa ndi Pastor J.J. Lim
Mothandizidwa ndi **Rev. David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **T. Mkwate**
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** komanso **Rev. Precious Kanyowa**

October 2010 Edition

Copyright © Gratia Dei Sola Media

KATEKISIMU WA ANA AANG'ONO KWAMBIRI
KUDZIWITSA KOYAMBA ZA CHIPHUNZITSO CHA BUKU LOPATULIKA

Lalembedwa ndi **Pastor J.J.Lim**
Mothandizidwa ndi **Pastor David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **T.Mkwate**
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** ndi **Rev. Precious Kanyowa**

Bukuli lasindikizidwa mu 2010 ndipo eni ake ndi a Pilgrim Covenant Church.

Chichewa version © 2012 Gratia Dei Sola Media
Lasindikizidwa ndi Grata Dei Sola Media
BlK 203B, Henderson Road , #07-07, Singapore 159546
Website: www.gdsmedia.org
Email: gdsmedia.sg@gmail.com

Palibe akuloledwa kusindikiza kapena kuchulukitsa buku ili ngakhale za mkatimu

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Synod ya Evangelical Presbyterian Church (EPC) ku Malawi ndi ku Mozambique inavomereza mu chaka cha 2012 kuti bukuli lizigwiritsidwa ntchito mu mipingo yawo yonse.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Mau Otsogolera

Kugwiritsa ntchito Katekisimu pofuna kuphunzitsa ana za Baibulo mu mpingo ndi njira yomwe yakhalapo kuyambira kale ndiponso yopambana. Ndipo ife, tatsatira njira imeneyi yomwe muli ma katekisimu okamba zambiri ya Baibulo komanso ena okhudza za chipangano komanso chikhulupiliro.

Ana athu adzayenera kuyamba kutsatira njira imeneyi ya katekisimu pamene afika potha kubwereza mayankho amene aperekedwa m'buku la oyamba kumene kuphunzira loyamba. Pasanafike apa, amayenera kukhala nawo mkalasi momwe amaphunzitsidwa funso limodzi pa sabata kuchokera mu *Katekisimu wa ana achichepere* komanso kumvetsera nkhani ya m'buku loyera/ lopatulika.

Ena a makolo athu, pofuna kuyambitsa ana awo pa gawo la ophunzira oyamba kumene apezapo kuti pamakhala chintchito chachikulu kuti mwana achoke pa kalasi la ana ongoyamba kumene kuyenda kufika pa gawo lapamwambali.

Ichi ndi chifukwa chake bukuli lalembedwa pofuna kuchepetsa vutoli komabe, choyenera kudziwa ndichakuti linalembedwa pogwiritsa ntchito *Catekisimu wa achichepere kwambiri.* Mwana ayenerabe kuphunzitsidwa kuloweza funso limodzi pa sabata koma palinso mafunso owonjezera kuti athandize makolo kuona kuti mwana wawo akumvetsetsa (kweni kweni) zomwe akuloweza.

Ngati mukugwiritsa ntchito bukuli, simukuyenera kuonetsetsa kuti mwana wanu akuloweza mayankho a mafunso a m'bukuli. Ngakhale izi zili chonchi, aphunzitsi a anawo m'makalasi adzagwiritsa ntchito mafunso omwewo pophunzitsa anawo. Dziwani kuti mwana wanu adzasangalala ndi maphunziro ake a mmakalasiwa ngati mwayamba kaye mwaonera pamodzi naye zomwe zili m'bukuli.

Mulungu adalitse kukangalika ndi kuyesayesa kwathu pophunzitsa ana athu mu njira yake ya Ambuye.

- Ps J. J Lim

PS. Chonde nenani zonse zomwe zalakwika kapenanso ndemanga zanu kuti tikonzenso moyenera ku <jjlim@pilgrim-covenant.com>

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.1 Anakupangani ndani?

Y: Mulungu.

Mafunso owonjezera:

1. Dzina lako ndani?
2. Anapanga (dzina la mwana) ndani?
3. Kodi Abambo ako anakupanga?
4. Kodi Amayi ako anakupanga?
5. Kodi Mulungu anakupanga?
6. (Pindani ka ndege ka mapepela ndikumuonetsa mwana) Anapanga ndege ya pepalayi ndani?
7. Anakupanga ndani?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.2 Ndi chiyani china chomwe Mulungu anapanga?

Y: Zinthu zonse.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi Mulungu anapanga (dzina la mwana) ?
2. Kodi Mulungu anapanga (mmene mwana amakuitanirani) ?
3. Kodi Mulungu anapanga mitengo?
4. (Onetsani chithunzi kapena chosema cha njobvu; bwerezani izi ndi nyama zina komanso tizirombo.) Kodi Mulungu anapanga njobvu?
5. Kodi Mulungu anapanga dzuwa? Mwezi? Nyenyezi? Dziko lapansi?
6. Mungandiuzeko zina zomwe Mulungu anapanga? (Osaonetsa kudabwa mwana akatchula zina zopangidwa ndi anthu monga galimoto komanso zolemera. Zisiyeni izi chomwechi ndipo mwanayo adzazindikira bwino yekha pamene akukula. Koma ngati mukuona kuti mwina mwanayo angamvetse, mufotokozereni kuti Mulungu anapanga zipangizo kenaka anthu omwe anapanga zinthuzo koma osachita izi mkalasi chifukwa zitha kuwasokoneza anawo mmalo mothandiza.)
7. Anakupanga ndani? Ndi chiyani china chomwe Mulungu anapanga? (Apa ndikubwerera ku yankho la Katekisimu)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.3 Nchifukwa chiyani Mulungu anapanga zinthu zonse?

Y: Chifukwa cha ulemelero wake

Mafunso owonjezera:

1. Kodi Mulungu anapanga mapiri? (Onetsani chithunzi cha phiri)
2. Kodi ukuganiza kuti phiri ndi lalikulu?
3. Kodi Mulungu ndi wamkulu kuposa phiri?
4. Kodi Mulungu anapanga mkango?
5. (Onetsani chithunzi cha mkango) Kodi mukuganiza kuti mkango ndi wamphamvu?
6. Kodi Mulungu ndi wamphamvu kuposa mkango?
7. (Onetsani duwa lenileni) Kodi Mulungu anapanga duwa ili?
8. Kodi mukuganizakuti duwali ndi lokongola?
9. Kodi Mulungu ndi ochenjera (wa nzeru) popanga duwali?
10. Mulungu akufuna kutionetsa kuti ndi wamkulu, wamphamvu, wanzeru komanso wabwino. Apa ndi chimodzimodzi kunena kuti: " Mulungu anapanga zinthu zonse chifukwa cha ulemelero wake."

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.4 Kodi tingadziwe za Mulungu kuchokera kuti?

Y: Kuchokera mu Baibulo (Buku lopatulika)

Mafunso owonjezera:

1. Ungandilozere Baibulo?
2. Kodi uli ndi Baibulo lako?
3. (Onetsani nyuzipepala.) Kodi tingaphunzire za Mulungu kuchokera ku nyuzipepala?
4. (Onetsani Buku lakusukulu. Onetsetsani kuti lisakhale lokamba za uzimu popewa kuwasokoneza ana) . Kodi tingaphunzire za Mulungu kuchokera m'bukuli?
5. (Onetsani mabuku ena angapo, magazini komanso Baibulo) Ndikuchokera m'buku liti la mabuku awa mmene tingaphunzilemo za Mulungu? (Ana asankhe pa mabukuwo)
6. Tingaphunzire chiyani kuchokera mu Baibulo? (Ana atha kupereka mayankho ambiri koma athandizeni kubwerela ku kuphunzira za Mulungu)
7. Kodi mukufuna kuphunzira za Mulungu? (Kambani za kuphunzira kuwerenga,kumvetsera bwino pamene Baibulo likuwerengedwa komanso zina..)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.5: Kodi Baibulo ndi chiyani?

Y: Mawu a mulungu.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi nkuchokera kuti komwe tingaphunzire za Mulungu?
2. (Bweretsani mulu wa mabuku ndi ma Baibulo angapo) Ungathe kusankha ma baibulo pa mulu wa mabukuwu?
3. Kodi tingaphunzire chiyani kuchokera mu Baibulo?
4. Analemba Baibuo ndani?(Apa patha kukhala mayankho osiyanasiyana potengera kamvetsedwe komanso kaphunzitsidwe ka mwana. Cholinga chenicheni nndichofuna kuwadziwitsa kuti ngakhale anthu 'oyera mu uzimu' analemba baibulo, mau ake onse ndi a Mulungu)
5. (Onetsani Baibulo) Kodi ndi mawu a ndani amene ali mu Baibulo?
6. (Onetsani buku) Kodi ndi mawu a ndani amene ali m'bukuli?
7. (Bwerezani funso 6, pogwiritsa ntchito mabuku osiyanasiyana monga ma magazini komanso ma baibulo)
8. Ngati Baibulo lili Mawu a Mulungu, tidzichita chiyani tikamaliwerenga?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F. 6: Kodi Amulungu alipo angati?

Y: Alipo Mulungu mmodzi yekha woona.

Mafunso owonjezera

1. (Ntchito ya ana yowerengera) Kodi uli ndi zala zammanja zingati? (Kodi uli ndi maso angati, makutu, manja – zinthu zomwezilipo kuposera chimodzi, ndi zina ?)
2. (Kupitiliza pa zowerengetsera) Kodi uli ndi abambo angati? (Nanga amayi, ndi zina)
3. Kodi mwaliwona dzuwa? Nanga pali mazuwa angati?
4. Kodi pali Amulungu angati?
5. Kodi mukudziwa bwanji kuti pali Mulungu mmodzi? (Baibulo limandiuza choncho)
6. Kodi tinganene kuti pali Amulungu ambiri? (Ana ena atha kunena kuti pali Amulungu ambiri koma zisiyeni kaye izi. Kambani nawo za Mulungu mmodzi WOONA)
7. Kodi tingati pali Amulungu atatu?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.7. Nanga bwanji mafano a mtengo kapena mwala?

Y: Amenewo ndi onama.

Mafunso owonjezera

1. Kodi Amulungu alipo angati?
2. Kodi mukudziwa zomwe zili zoona kapenanso zonama? (Fotokozani pogwiritsa ntchito mawu monga ' zeni zeni' komanso 'zabodza')
3. (onetsani nsomba yeniyeni ili m'botolo komanso tinsomba tina tosema kapena tapepala.) Kodi ndi iti yomwe ili yeni yeni? Ndi ziti mwa izi zomwe zili zabodza?
   Bwerezani ndi zinthu zina monga masamba kapena zipatso. Kumbukirani kusagwiritsa ntchito zithunzi za izi ngakhale chiri chapafupi kujambula tsamba kapena nsomba nkudzidula bwino kuchokera pomwe mwajambulapo)
4. Kodi Amulungu owona alipo angati?
5. Kodi nanga mafano osema kuchokera kumtengo kapena mwala? (Mutha kugwiritsa ntchito zithunzi apa ngati ndi kotheka)
6. Anthu ambiri amapemphera kwa Amulungu onama. Kodi tipemphere kwa Amulungu onama? Kodi angakumve? Kodi angathandize anthu amne akupemphera kwa iwo?
7. (Kuti mupereke chitsanzo chothandiza kuti izi zimveke ,gwiritsani ntchito chidole kapena mwatche. Afunseni anawo ngati angathe kuchipanga chidolechi kuti chiyende pongochilankhula?)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.8. Kodi pa Mulungu pali anthu angati?

Y. Atatu

Mafunso owonjezera

(Mafunso otsatirawa apangidwa moti athe kuthandiza makolo kuti athe kuwonetsetsa kuti ana akumvetsetsa bwino lomwe kuti pali anthu atatu amene umodzi wawo umatchedwa Mulungu. Anthu ena atha kumayesa kuti mafunsowa akupereka chithunzi cholakwika cha chiphunzitso cha utatu woyera. Komabe, dziwani kuti, mafunsowa sanakonzedwe kuti afotokoze tchutchutchu wa utatu woyerawu. Chofunika ndi choti ana athu athe kuona bwino kuti mbali ina Mulungu ndi mmodzi ndiponso anthu atatu mbali ina.)

1. *Kodi uli ndi manja angati?*
2. Kodi dzanja lililonse liri ndi zala zingati?
3. Kodi kwanu kuli mabanja angati? (Funsoli lingakhale lovuta kwa ana amene sakudziwa bwino tanthauzo la banja)
4. (Ngati mwana akutha kuyankha funso 3.) Kodi ndi anthu angati amene ali m'banja mwanu?
5. Kodi pali Amulungu angati?
6. Kodi ndi anthu angati amene ali pa Mulungu?
7. Kodi pali anthu awiri (anayi, asanu ndi ena) okha pa Mulungu?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.9. Kodi ndi anthu ati amene ali pa Mulungu?

Y. Atate, Mwana ndi Mzimu woyera.

Mafunso owonjezera

1. Kodi pali Amulungu angati?
2. Kodi pali anthu angati pa Mulungu?
3. Anthu awa ndi ndani?
4. Kodi mukudziwa amene ali Atate? (Awa ndiye Atate athu a kumwamba. Timalankhula nawo tikamapemphera)
5. Kodi Atatewa ndi Mulungu?
6. Kodi mukudziwa dzina la Mwanayo?
7. Kodi Mwanayo ndi Mulungu?
8. Nanga Mzimu woyerawo ndi Mulungu?
9. Kodi pali Amulungu angati?
10. Kodi pali anthu angati pa Mulungu?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.10. Kodi Mulungu ali kuti?

Y. Mulungu amapezeka paliponse.

Mafunso owonjezera

1. Kodi tingaphunzire za Mulungu kuchokera kuti?
2. Kodi pali Amulungu angati?
3. Nanga bwanji mafano a mtengo komanso mwala?
4. Kodi mafano amapezeka kuti? (M'makachisi, mmalo ogulitsiramo zakumwa, kunyumba kwa agogo, ndi kwina..)
5. Kodi Mulungu ali kuti?
6. Kodi Mulungu ali kumwamba?
7. Kodi Mulungu ali pompano?
8. Kodi ali ku Australia (china, America, zambia , ndi kwina)
9. Kodi utapita ku phiri (pansi pa nyanja, ku mwezi) Mulungu angakhaleko?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.11. Kodi mungamuone Mulungu?

Y. Ayi. Koma Iye amandiona ine.

Mafunso owonjezera:
(Mafunso otsatirawa akonzedwa kuti athe kuthandiza mwana kuti amvetsetse kuti ngakhale sangamuone Mulungu, Iye amawaona ndipo amadziwa zonse zomwe akuchita anawo . Ana ambiri a msinkhu uwu amakhala kuti sanafike poganiza kuti zomwe iwo sangazione ndi maso awo zitha kukhalapo kapena ayi. Izi sizitanthauza kuti anawa amalinganitsa kukhalapo kwa chinthu ndi kuwona koma kuti satha kudziwa kuti kodi tikati '' kukhalapo kwa chinthu'' tikutanthauza chiyani. Pachifukwa ichi, mwana sangathe kufunsa zambiri za kukhalapo kwa Mulungu monga mmene sangafunsire zina ndi zina zomwe amauzidwa. Kuonjezera apa, sitinaike dala nkhani yoti zomwe sitingaziwone sizingakhalepo powopa kusokoneza. Koma ngati mwana afunsa, mphunzitsi atha kumuyankha potenga ndalama ya chitsulo nkuiyika m'manja kenaka nkuibisa mogwira ndi zanja lomwelo nafunsa mwanayo ngati akuiwona. Mwana akayankha kuti sakuiwona, mphunzitsi afotokoze kuti ngakhale sakuiwona ilipo mmanjamo. Komabe izi zimakhala zosokoneza maka kwa mwana.)

1. Tingadziwe za Mulungu kuchokera kuti?
2. Kodi pali Amulungu angati?
3. Kodi Mulungu ali kuti?
4. Kodi ali m'chipinda muno?
5. Kodi mukumuwona?
6. Kodi Mulungu amadziwa dzina lanu?
7. Kodi Mulungu amadziwa zomwe mukuchita?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.12. Kodi ife ndiosiyana bwanji ndi nyama?

Y. Chifanizo cha Mulungu chili mwa ife.

Mafunso owonjezera:

1. Anthu ena amanena kuti anyamata ndi atsikana samasiyana ndi anyani komanso abulu. Kodi inu ndinu osiyana ndi anyani komanso abulu?
2. Kodi inu ndi osiyana bwanji ndi anyani komanso abulu? (mufunse limodzi ndi kuti; kodi inu ndiwosiyana bwanji ndi nyama? Chifanizo chake cha Mulungu chili mwa ine.)
3. Kodi ukutanthauza chiyani ukati "chifanizo cha mulungu chili mwa iwe" ?
   (Ganizo lanu: zikutanthauza kuti uli ndi mzimu. Nyama zilibe mzimu)
4. Kodi mukudziwa kuti mzimu ndi chiyani? (Ganizo lanu: ndi chinthu chomwe sungachiwone. Chifukwa chooti uli ndi mzimu, umatha kuganiza, kulankhula, kumwetulira, kupemphera komanso kudziwa pakati pa chabwino ndi choipa)
5. Kodi mukuganiza kuti nyani ali ndi mzimu?(Dziwani: Anthu ena a zachipembezo amati nyama zili ndi mizimu yawo koma osati yoti nkuganiza bwino bwino, chonde musasokoneze nazo ana izi. Nthawi zonse, kambani za mzimu umodzi wopezeka mwa munthu osati nyama ayi)
6. Mukudziwa bwanji kuti nyani alibe mzimu? Munaonapo nyani akupemphera? Munawonapo nyani akumwetulira? Nanga nyani anakupatsanipo moni wa pakamwa?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.13. Kodi munthu woyamba anali ndani?

Y. Adamu

Mafunso owonjezera

1. Kodi mukudziwa pamene mungapeze dzina loti ‚Adamu' m'Baibulo? (M'masamba oyambilira)
2. Kodi Adam anali nyama? Nanga anali wamwamuna kapena wamkazi?
3. Kodi mukudziwa mmene Adam ankawonekera? (Ayi, analipo zaka zambiri zapitazo. Analipo musanabadwe. Abambo anu asanabadwe. Aliyense asanabadwe.)
4. Kodi Mulungu anamupanga bwanji Adam? (Anamupanga kuchokera ku dothi lapansi)
5. Kodi mungathe kupanga munthu ndi dothi lapansi? (Zina zomwe mungathe kuchita: Umbani kachidole kamunthu kuchokera ku dothi kuti ana amvetse)
6. Kodi Mulungu angapange munthu kuchokera ku dothi lapansi? (Inde; ndipo anamupatsa mzimu)
7. Mulungu anapanganso mkazi. Kodi mukudziwa dzina lake?
8. Kodi muli ndi agogo anu Aamuna komanso Aakazi? Nanga mukudziwa kuti Adam ndi Eva ndi agogo a akulu a agogo athu ndi agogo awo ndiponso iwo agogo awo?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.14. Kodi Adam anali wotani pamene ankamulenga?

Y. Wabwino

Mafunso owonjezera:
(Mafunso awa akukamba za chabwino ndi choipa zomwe zili zovuta kumvetsa ana a ang'ono kwambiri. Pamsinkhu uwu atha kumvetsa kuti kuba komanso mwano ndi zoipa koma nkovuta kumvetsa kuti iwo komanso ena onse ndi ochimwa. Tiyesa kukambako za izi mmafunso otsatirawa koma pakadali pano, anawa adziwe kuti Adam anali womvera Mulungu)

1. Kodi wakuba ndi wabwino kapena woipa? Nanga wakupha ndi wabwino kapena woipa?
2. Kodi wakuba ndi woipa bwanji? (chifukwa amaphwanya lamulo)
3. Nanga wapolisi ndi wabwino kapena woipa?(vomerani yankho loti "wabwino")
4. Kodi wapolisi ndi wabwino chifukwa chiyani? (chifukwa amasunga lamulo)
5. Kodi (Dzina la mwana) ndiwabwino kapena woipa? (Ambiri ayankha kuti wabwino ngakhale makolo atawakumbutsa zina za iwo! ndi mmene tinabadwila! Koma osawatsutsa pakadali pano, gwiritsani yankholi kuti mufunse funso lotsatira) Kodi ndiwewabwino nthawi zonse? (Ayi)
6. Ndi nthawi iti yomwe umakhala woipa? (Kapena, umakhala wabwino pamene sunamvere abambo kapena amayi?)
7. Nanga ndichifukwa chiyani Adam anali wabwino? (chifukwa anali womvera Mulungu nthawi zonse

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.15. Kodi Adam anakhalabe wabwino?

Y. Ayi, anachimwa

Mafunso owonjezera;

1. Kodi Adam anali wotani pamene amamulenga? (anali wabwino)
2. Nchifukwa chiyani anali wabwino?(Mulungu anamupanga kukhala wabwino. Amamvera Mulungu nthawi zonse)
3. Munali mitengo iwiri ya zipatso mmunda wa Edeni. Kodi mukudziwa mayina ake a mitengoyi?
4. (Onetsani chipatso cha apulo kapena mango lopsa bwino) Mtengo wa chipatso chodziwitsa zabwino ndi zoipa unabereka chipatso ngati ichi. Chikuoneka chokoma?
5. Kodi Adam ndi Eva analoledwa kudya ichi? (ayi)
6. Kodi Adam anadya chipatsochi? (inde)
7. Kodi zinali zoyenera kuti iye achite izi?
8. Kodi podya chipatsochi anasonyeza kumvera Mulungu? (ayi)
9. Fotokozani kuti pamene simumvera malamulo kapena malangizo, mumachimwa. Tiona zambiri za izi mu funso lathu lotsatira)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.16. Kodi tchimo nchiyani?

Y. Kusamvera Mulungu.

Mafunso owonjezera:

1. Mulungu anauza Adam kuti asadye chipatso chochokera mu mtengo wodziwitsa chabwino ndi choipa. Kodi Adam anamvera?
2. Pamene Adam sanamvere Mulungu, anachimwa. Kodi mumadziwa kuti mumachimwa pamene simunamvere Mulungu?
3. Kodi munachimwapo? (ngati yankho lili 'eya',funsani chomwe anachita ndipo ngatilili 'ayi' perekani zitsanzo za zinthu zomwe munthu angachite kuti achimwe kuti mupeze yankho loyenera)
4. Kodi mumadziwa kuti Mulungu anatipatsa malangizo a zinthu zomwe tiyenera kuchita kapena kusachita? Kodi izi zimapezeka kuti?
5. Kodi mungaperekeko zina mwa zitsanzozi?
6. Mukuganiza kuti Mulungu adzakondwera nanu pamene simunamumvere?
7. Kodi muyenera kuchita chiyani pamene mwadziwa kuti mwachimwila Mulungu?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.17. Kodi chilango cha uchimo nchiyani?

Y. Imfa

Mafunso owonjezera:
(Funsoli likuyambitsa kukambapo za imfa, koma pakuti nkhani yeniyeni ili pa za uchimo, tisiya kaye za imfa mpaka mu funso linalo)

1. Kodi mukapanda kumvera abambo anu, abambo anuwo amakupangani chiyani? (ngati mwana wayankha kuti, 'amandilanga' kapena lina lopitila komweko, funsani kuti,'amakulanga bwanji?')
2. Ukuganiza kuti ndibwino kusamvera abamo ako? Ndibwino kuti abambo ako akulange?
3. Adamu sanamvere Mulungu. Sanamumvere Mulungu bwanji? (Pakudya chipatso chomwe analetsedwa chodziwitsazabwino ndi zoipa)
4. Kodi kunali koipa kuti Adamu asamvere Mulungu?(Awuzeni kuti ndi chinthu choopsa kwambiri kusamvera Mulungu kusiyana ndi Kusamvera makolo anu.)
5. Kodi mukuganiza kuti Mulungu anakwiya ndi Adam chifukwa chakuti sanamumvere?(ngati mwana wayankha kuti ,'ayi' mfuseni kuti,' kodi ukapanda kumvera abambo ako, iwo amasangalala?)
6. Kodi mukudziwa mmene Mulungu anamulangila Adam?(Anamuthamangitsa mmunda wa Eden ndipo anamuuza kuti adzafa)
7. Kodi Adam anamwalira chifukwa chiyani? (chifukwa anachimwa)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.18. Kodi chinachitika nchiyani Adam atachimwa?

Y. Anthu onse ochokera kwa iye amamwalira

Mafunso owonjezera:
(Funsoli likukamba kwambiri za imfa ndipo ana akuyembekezeka kukhala ndi kamvetsedwe ka tanthauzo la imfa molingana ndi zimene akumana nazo mmiyoyo mwawo pankhaniyi. Mwachitsanzo, mwana amene anataya wokondedwa kapena anatengedwako ku mwambo wa maliro atha kumvetsa bwino lomwe kusiyana ndi amene izi sizinamuchitikirepo. Ndipo pa chifukwa chakuti anawa amamvetsetsa mosiyana pa nkhaniyi, mafunso a m'ndimeyi akonzedwa potengera ganizo loti mwana wina mgululo akudziwako za imfa ndiponso pofuna kuti nkhaniyi imveke bwino, imfa ya nyama ndi yomwe ikukambidwa mmafunsowa kuti ana asasokonezeke komabe ngati kuli kotheka, imfa ya anthu itha kukambidwa.)

1. Kodi unawaonako abambo awo a agogo ako? Ukuziwa chomwe chinawachitikira kuti usawaone?(Mutha kulisintha funso kuti likambe za wina amene mwanayo/anawo anamuonapo ngati nkotheka.)
2. Unaonapo munthu womwalira? Anali ndani?Ankalankhula? Amatha kusuntha dzanja lake?
3. Kodi ukudziwa kuti tsiku lina tonse tidzafa?(Pokhapokha Ambuye atabwera msanga,ife tonse tidzamwalira)
4. Kodi ukudziwa chifukwa chimene tonse tiyenera kumwalira? (Chifukwa Adam anachimwa. Chifukwa tonse ndife ochimwa)
5. Kodi ukuganiza kuti tsiku lina nawe udzamwalira? Chifukwa chiyani? (Chifukwa Adam anachimwa. Chifukwa ndine wochimwa ndipo mphoto ya uchimo ndi imfa – Onani funso 17. Kumbukirani kuti imfa sichilango kwa ake osankhika, koma chiyambi cha kulowa mu ulemelero wake wa Mulungu. Komabe , dziwani kuti pakadali pano ndi zovuta kuwafotokozera bwino anawa za izi ndipotidzakamba bwino mu funso 24)
6. Kodi ukudziwa zomwe zitadzachitike ukadzamwalira? (Thupi lako lidzapita kumanda, koma mzimu wako udzapita kumparadizo kapena jahena. Fotokozani mwachidule za jahena ndi mparadizo)
7. Kodi ukudziwa amene adzapite ku mparadizo? (Okhawo amene amakhulupilira mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.19. Ndani angatipulumutse ife ku imfa ndi tchimo?

Y. Ambuye Yesu Khristu yekha.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi mukukumbukira mmene Adam anachimwira?(Sanamvere Mulungu. Anadya chipatso choletsedwa cha mumtengo wodziwitsa chabwino ndi choipa.) Chinachitika ndi chiyani Adam atachimwa? (Anthu onse obadwa mwa iye amamwalira)
2. Kodi iwe ndiwe ochimwa?
3. Kodi iwe udzamwaliranso?
4. Kodi udzapita kuti ukadzamwalira? (Thupi langa lidzapita m'manda koma mzimu wanga udzapita ku paradizo kapena jahena)
5. Kodi ndi kuti komwe ungafune kupitako utamwalira?
6. Angakutengere kumeneko ndi ndani?
7. Ambuye wathu Yesu khristu ndi amene angatitengere ku paradizo chifukwa ndi iye yekha amene angatipulumutse ife ku imfa ndi tchimo.
8. Kodi mumakhulupilira mwa Ambuye wathu Yesu Khristu?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.20. Kodi Ambuye Yesu Khristu ndi ndani?

Y. Mwana wa Mulungu.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi angatipulumutse ife ku imfa ndi tchimo ndi ndani? (Ambuye Yesu Khristu Yekha)
2. Kodi mukudziwa kuti Ambuye Yesu Khristu ndi ndani?
3. Kodi mumuonapo Ambuye Yesu Khristu? (Ayi; Anali padziko pano zaka zambiri zapitazo)
4. Kodi tingawerenge za Ambuye Yesu Khristu kuti? (Mu baibulo)
5. Kodi ungandiuzeko zinthu zina zomwe Ambuye Yesu anachita? (Anachiza odwala; Anapangitsa osaona kuona; Anaukitsa akufa; Anakhalitsa bata namondwe pamadzi; Anauka kwa akufa....ndi zina zotero)
6. Kodi ungathe kuchita izi?
7. Kodi ukudziwa chifukwa chimene Yesu ankatha kuchita zinthu izi? (chifukwa ndi Mulungu, kapena chifukwa ndi mwana wa Mulungu)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.21. Kodi Ambuye Yesu anachimwapo?

Y. Ayi, Iye yekha sanachimwepo.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi ukukumbukira kuti tchimo ndi chiyani? (Kusamvera Mulungu)
2. Kodi Adamu anachimwa? Nanga anachimwa bwanji?
3. Ndi njira zanji zina zomwe munthu angachimwire?
4. Munthu amene amachita tchimo ndi wochimwa. Kodi iwe ndi wochimwa? Nanga amayi ako ndi wochimwa? Nanga abambo? Aphunzitsi? Abusa?
5. Kodi Ambuye Yesu Khristu ndiwochimwa?
6. Kodi ukudziwa munthu amene sanachimwepo?
7. Kodi nchifukwa chiyani Ambuye Yesu sanachimwepo ndipo sadzachimwa? (chifukwa ndi mwana wa Mulungu)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.22. Kodi Yesu anachitira anthu ake chiyani?

Y. Anafa chifukwa cha machimo a anthuwo.

Mafunso owonjezera:
(Ambuye Yesu Khristu anakhala ndi moyo, anazunzika ndiponso anafera anthu ake. Ngakhale izi zili chonchi, nkhani yathu yeniyeni ili pa za imfa yake ya Yesu)

1. Kodi ukukumbukira kuti chilango cha imfa ndi chiyani? (Funso.17 -imfa)
2. Kodi Ambuye Yesu anachimwapo? (Funso. 21 – Ayi; Iye yekha sanachimwepo)
3. Kodi Yesu anayenera kulangidwa?
4. Kodi Yesu anayenera Kufa?
5. Kodi anthu a Mulungu anachimwa?
6. Kodi anthu a Mulungu anayenera kufa ndikupita ku Jahena?
7. Koma anthu a Mulungu akupita ku paradizo. Ukudziwa chifukwa chake?
8. Ambuye Yesu Khristu anafera pa mtanda. Kodi ukudziwa chifukwa chimene anafera?
9. Kodi Ambuye Yesu anachitira chiyani anthu ake?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.23. Kodi Ambuye Yesu anakhalanso ndi moyo?

Y. Inde; Anaukanso ku imfa nakwera kumwamba.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi unawonapo munthu womwalira?
2. Kodi munthu womwalira angauke ndi kuyenda?
3. Nanga kodi adotolo angamuchititse muthu womwalira kuti akhalenso ndi moyo?
4. Kodi ukudziwa chifukwa chimene Ambuye Yesu anafa koma anaukanso?
5. Kodi ukudziwa kuti anakhala masiku angati ali mmanda? Nanga anauka tsiku lachingati?
6. Kodi ungatchule mayina a amzake a Yesu amene anamuona Yesu atauka kwa akufa?
7. Kodi Yesu anakwera kumwamba patatha masiku angati chiukire kwa imfa?
8. Kodi ukudziwa kuti Yesu anakwera bwanji kupita kumwamba?
9. Kodi nawenso ungakwere kupita kumwamba?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.24. Kodi Mulungu adzalanga anthu ake chifukwa cha tchimo?

Y. Ayi, Yesu analangidwa chifukwa cha iwo.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi unavutitsapo makolo ndipo amayi anakukwapula?
2. Atakukwapula amayi, kodi abambo ako anakukwapulanso?(Konzekerani kumva mayankho omwe simumayembekezera, koma atsogolereni ku ganizo loti pamene chilango chaperekedwa chinanso sichiyenera kuperekedwa)
3. Kodi mukuona kuti anthu a Mulungu ayenera kulangidwa? (Inde , chifukwa Adamu ,kholo lathu loyamba anachimwa ndipo baibulo limatiuza kuti tonse tidachimwa chifukwa cha iye.)
4. Koma ukudziwa komwe anthu a Mulungu atadzapite akadzamwalira?
5. Ndichifukwa chiyani mukuganiza kuti sadzapita ku jahena?
6. Kodi mukuona kuchuluka kwake kwa chikondi cha Ambuye Yesu kwa ife?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.25. Kodi ntchito ya Ambuye Yesu imabwera bwanji kwa anthu ake?

Y. Imabwera ndi Mzimu woyera.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi mungakumbukire zomwe Ambuye Yesu Khristu anachitira anthu ake?
2. Pamene Ambuye Yesu anamwalira , anabweretsa mphatso kwa anthu ake. Kodi mukudziwa dzina la mphatso imeneyi? (Moyo wosatha)
3. Kodi utafuna kumupatsa mphatso mzako amene amakhala kutali kwambiri, ungatani? (Kutumiza kudzera ku ofesi yotumizira katundu)
4. Ambuye Yesu anapita kumwamba komwe kuli kutali ndi ife. Kodi mukudziwa mmene Ambuye Yesu amatumizira mphatso yomwe anatigulira ife? (Kudzera mwa Mzimu woyera)
5. Kodi mukudziwa kuti mzimu woyera ndi ndani? (Mulungu)
6. Kodi mungauwone Mzimu woyera, Nanga mungamugwire Mzimu woyera?
7. Sindingathe kuona kapena kugwira mzimu woyera, koma amandipangitsa ine kukhala wosangalala. Mukudziwa chifukwa chake?(Fotokozani mmene mphatso zimabweretsera chisangalalo.)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.26. Kodi Mzimu Woyera amatani?

Y. Amapereka Chikhulupiliro.

Mafunso owonjezera:

1. Yohane ndi M'khristu. Yudasi si M'khristu. Kodi mukudziwa chimene Yohane ali nacho chomwe Yudasi alibe? Kodi ndi ndalama? Kodi ndi nyumba? Kapena ndi chikhulupiliro?
2. Baibulo limati; ''pakuti muli opulumutsidwa mwa chisomo chakuchitidwa mwa chikhulupiliro ndipo ichi ndichosachokera kwa inu''(Aefeso 2v8)
3. Kodi Yohane ayenera kulipila kuti apeze chikhulupilirochi? (Ayi)
4. Analipira ndani (Ambuye Yesu Khristu)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.27. Kodi chikhulupiliro ndi chiyani?

Y. Kukhulupilira mwa Yesu Khristu.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi mukukumbukira zomwe Mzimu woyera umachita? (Umapereka chikhulupiliro)
2. Kodi mukudziwa kuti chikhulupiliro nchiyani?
3. Kodi tikati kukhulupilira mwa Khristu tikunena chiyani? (Uku ndiko kukhulupilira kuti iye ndi mwana wa Mulungu ndipo anafa chifukwa cha machimo anga kuti andipange ine kukhala mwana wa Mulungu)
4. Kodi aliyense ali ndi chikhulupiliro? (Ayi,amene si akhristu alibe chikhulupiliro)
5. Kodi iwe uli ndi chikhulupiliro? Nanga umakhulupilira mwa khristu?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.28. Kodi tingadziwe bwanji kuti timakhulupilira mwa Khristu moonadi?

Y. Zochita zathu zimakhala zabwino ndi zolungama.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi ndi anthu angati pa dziko lapansi amene amanena kuti ndi a khristu? Kodi ndi khumi (10)? Zana (100)? kapena chikwi (1000)? (kapena kuposera apo)
2. Kodi mukuganiza kuti aliyense wonena kuti ndi m'khristu amakhulupiliradi mwa Yesu moona? (Ayi, Yudasi Isikarioti komanso Simon Magusi ankadzitcha a khristu koma sanali okhulupilira moonadi)
3. Kodi alipo ambiri lero amene siokhulupilira oonadi? (Inde, Ambuye amatiuza kuti ambiri amene amamutchula kuti Ambuye ,Ambuye, patsiku lomaliza adzakanidwa ndi Iye.)
4. Kodi ukudziwa kumene okhulupilira muchoonadi adzapite akadzafa? Nanga komwe okhulupilira monama adzapite akadzafa?
5. Kodi ungadziwe bwanji ngati ukhulupilira moonadi mwa Khristu?
6. Kodi ntchito zabwino ndi ziti?(Kumvera malamulo a Mulungu, Kuthandiza anthu ena pamene avutika)
7. Kodi umakhulupilira mwa Khristu?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.29. Kodi anthu ake a Yesu Khristu ndi ati?

Y. Mpingo.

Mafunso owonjezera:
(Dziwani kuti mafunsowa akukamba za mpingo kapena tchalichi chooneka ndi maso osati mpingo wosaoneka poopa kuwasokoneza ana a msinkhu omwe bukuli lalembedwera)

1. Kodi anthu amene amakhulupilira mwa Khristu amatchedwa ndani? (Akhristu)
2. Kodi anthu onse a mdziko muno ndi akhristu?
3. Kodi akhristu mungawapeze kuti?
4. Kodi anthu a Mulungu amapezeka mu mpingo kapena tchalichi chilichonse? (Ayi, pali mipingo yoona komanso ina yabodza kapena yonama)
5. Ndi mmipingo iti yomwe sitingapezemo anthu a Mulungu? (Mpingo wa Katolika, mpingo wa chimormoni, Mpingo wa Mboni Za Yehova, Mpingo wa Chisalamu ndi ina)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.30. Kodi Khristu anapereka chiyani kwenikweni ku Mpingo?

Y. Ubatizo komanso Mgonero wa Ambuye.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi munabatizidwa? Ungafotokoze mmene zimakhalira pobatizidwa?
2. Kodi unaonapo ana komanso akulu akubatizidwa?
3. Kodi ukudziwa kuti Mgonero wa Ambuye ndi chiyani? Ungaufotokoze?
4. Kodi umadya mkate komanso kumwa vinyo pa mgonero wa Ambuye?
5. Kodi ungafune kudya mkate ndiponso kumwa vinyo?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.31. Kodi Ubatizo umationetsa chiyani?

Y. Umationetsa kuti ndife anthu ake a Khristu

Mafunso owonjezera;

1. Kodi mukudziwa chomwe madzi a ubatizo amatanthauza? (Mwazi komanso Mzimu wa Yesu Khristu)
2. Kodi anthu onse a m'dziko lapansi anasamba m'mwazi wa Khristu? (Ayi)
3. Kodi ndi ndani amene amasambitsidwa m'mwazi wa Khristu? (Anthu a Mulungu)
4. Kodi aliyense pa dziko lapansi ali ndi Mzimu wa Khrisu? (Ayi)
5. Kodi anthu amene ali ndi Mzimu wa Khristu ndi ndani? (Anthu a Mulungu)
6. Kodi Ubatizo ukutionetsa chiyani?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.32. Kodi Mgonero wa Ambuye umationetsa ife chiyani?

Y. Umationetsa kuti Khristu anatifera ife.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi pa Mgonero wa Ambuye pamachitika chiyani?
2. Kodi nanga mkate umaimira chiyani? (Thupi la Khristu)
3. Kodi nanga kutema kwa mkate kumatanthauza chiyani? (Thupi la Yesu kukutemedwa chifukwa cha ife)
4. Kodi vinyo wa pa Mgonero wa Ambuye amaoneka wamtundu wanji?
5. Kodi nanga vinyoyu amaimira chiyani? (Mwazi wa Yesu Khristu)
6. Kodi thupi la Khristu linatemedwa komanso mwazi wake kukhetsedwa liti?
7. Kodi Mgonero wa Ambuye umationetsa chiyani?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.33. Kodi mtsogoleri wa mpingo ndi ndani?

Y. Ambuye Yesu Khristu.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi Abusa ndi mtsogoleri wa mpingo?
2. Kodi akulu a mpingo ndi atsogoleri a mpingo?
3. Kodi Atumiki ndi atsogoleri a mpingo?
4. Kodi Ambuye wathu Yesu Khristu ndi mtsogoleri wa mpingo?
5. Ngati Ambuye Yesu ndi mtsogoleri wa mpingo, tichite chiyani? (Timutumikire komanso kumumvera)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.34. Kodi ndi maudindo ati amene Khristu wasankha mumpingo?

Y. Akulu a mpingo komanso Atumiki.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi mumpingo mwathu muli akulu a mpingo anagati?
2. Kodi akulu a mpingowa amatani? (Kulamulira komanso kuphunzitsa mpingo)
3. Kodi mu mpingo mwathu muli atumiki angati?
4. Kodi atumiki amenewa amatani? (Amagawa chisomo cha Khristu poyang'anira ndi kusamalira chuma mu mpingo)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.35. Kodi mpingo wa Khristu unafika pokhala wabwino ndi wopanda cholakwika?

Y. Ayi, sunafike

Mafunso owonjezera:

1. Kodi ukudziwa zofunika kuti chinthu kapena munthu akhale wabwino ndi wopanda cholakwika?
2. Kodi ndiwe osalakwika?
3. Ndi chifukwa chiyani ukuti sindiwe osalakwika?
4. Kodi mpingo wa Khristu ndi wosalakwika lero?
5. Kodi timadziwa bwanji kuti mpingo siwabwino ndiponso wazolakwika?
6. Kodi ukuganiza kuti mpingo wabwino ndi wopanda zolakwika uzakhala wotani?
7. Kodi ife tidzakhala opanda cholakwika tsikulina? (Inde; popeza buku lopatulika limatiuza choncho)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.36. Kodi mpingo udzakhala wopanda cholakwika liti?

Y. Panthawi ya kuuka kwa akufa.

Mafunso owonjezera:

1.Kodi munapitapo kumanda?

2. Kodi mukudziwa aliyense amene anaikidwa kumanda?

3. Kodi mukudziwa zomwe zinachitika ndi thupi lake? (Linasanduka dothi)

4. Kodi ukudziwa kuti tsiku lina akufa onse adzasanduka amoyo?

5. Tsiku limenelo ndiye tsiku la kuuka kwa akufa. Nena kuti ' Kuuka kwa akufa'

6. Kodi kuuka kwa akufa ndi chiyani? (Ndipamene aliyense wakufa adzasandusidwa kukhalanso wamoyo)

7. Patsikulo onse amene adzakhale ali moyo adzaona matupi awo akusinthika. Koma amene anafa kale adzapatsidwa matipi ena.

8.Kodi ukuganiza kuti tsikulu lidzakhala tsiku losangalala? (Lidzakhala loasangalala kwa okhawo amene ali aKhristu)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F. 37. Kodi pa tsiku louka kwa akufa pamachitika chiyani?

Y. Khristu amaweruza anthu onse.

Mafunso owonjezera:

1.Kumbukirani kuti Kuuka kwa akufa ndi chiyani? (Akufa adzaukitsidwa)

2. Kodi tsiku louka kwa akufa lidzakhala losangalatsa? (Lidzakhala losangalatsa kwa akhristu, koma tsiku lokhumudwitsa kwa omwe si akhristu)
3. Kodi ukudziwa chifukwa chake akhristu atadzakhale osangalala pamene omwe si akhristu adzakhale okhumudwa? (chifukwa Yesu adzaweruza anthu onse)
4. Kodi tikati Yesu Khristu adzaweruza anthu onse tikutanthauzanji? (Izi zili ngati kuti Yesu adazachonga zonse zomwe aliyense anachita monga mmene aphunzitsi amachongera zolemba zathu zomwe anatipatsa kuti tikalembere kunyumba)
5. Khristu adzawapatula anthu kukhala magulu awiri. Nkhosa mbali imodzi yakumanja ndiponso mbuzi mbali imodzi yakumanzere. Akhristu ndiye nkhosa, tidzakhala kumanja. Kodi udzakhala kuti? Kumanja kapena kumanzere?
6. Nkhosa ndi zimene Khristu amapulumutsa ndipo mbuzi ndizo zotsapulumutsidwa. Kodi ndiwe mbuzi kapena nkhosa?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.38. Kodi chitazachitike ndi chiyani kwa anthu amene Khristu wawapulumutsa?

Y. Adzakhala ndi iye limodzi mpaka kale kale ku mparadizo.

Mafunso owonjezera:

1. Kumbukirani kuti pouka kwa akufa, Khristu adzapatula nkhosa zake kuzilekanitsa ndi mbuzi?
2. Kodi mbuzi ndi ndani? (Ndi amene Khristu adzawalange)
3. Kodi nkhosa ndi ndani? (Awa ndi amene Khristu adzawapulumutse)
4. Kodi ndiwe nkhosa kapena mbuzi?
5. Kodi chizachitike ndi chiyani kwa amene Khristu adzawapulumutse? (Khristu adzawatenga kumwamba kumene adzakhale nawo mpaka kalekale)
6. Kodi mukudziwa kuti kumwamba nkooneka bwanji?
7. Kodi mukufuna kudzapita kumwamba?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.39. Kodi chidzachitike ndi chiyani kwa amene Khristu sanawapulumutse?

Y. Adzafa mpaka kalekale ku moto wa jahena.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi ukukumbukira kuti pa tsiku louka kwa akufa, onse amene anafa adzapatsidwa matupi awo?
2. Akhristu adzakondwera kumwamba ndi thupi lomwe lidzakhale lopanda mabala komanso ululu. Kodi ungafune thupi ngati limeneli?
3. Nanga bwanji anthu omwe si akhristu? Kodi ukudziwa thupi lomwe atadzakhale nalo? (adzakhala ndi thupi lomwe litazakhale ndi ululu komanso kusakondwa)
4. Adzaponyedwa kumoto wa jahena ndi thupi lawo. Kodi ukudziwa chifukwa chake? (Chifukwa amachimwira Mulungu ndi thupi komanso Mzimu wawo, choncho Mulungu adzalanga thupi komanso Mzimu wawo.)
5. Kodi ukudziwa kuti jahena ali ngati chiyani?
6. Kodi ukuganiza kuti winawake azakhala osangalala ku Jahena?
7. Kodi ungadzafune utapita ku Jahena? Ngati ayi, uyenera kuchita chiyani?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.40. Kodi lamulo la Mulungu timalipeza kuti?

Y. M'Malamulo khumi a Mulungu.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi amayi kapena abambo ako anakupatsa malamulo akuti udzitsatira?
2. Mulungunso ali ndi malamulo ake kwa ife. Kodi ukudziwa kuti malamulowa amatchedwa chiyani? (Malamulo khumi a Mulungu)
3. Lamulo la Mulungu lili mu malamulo ake khumi. Kodi mukudziwa kumene mungapeze malamulowa m'buku lopatulika? (Exsodo 20)
4. Malamulo khumiwa ndiofunika kwambiri kwa ife ngati mmene madzi amakhalira kwa nsomba kuti zikhale moyo. Kodi ukudziwa zomwe zingachitike titaichotsa nsomba mmadzi nkuiyika pamtunda?
5. Ngati sitisunga Malamulo a Mulungu tili ngati nsomba zomwe zatulutsidwa mmadzi. Ukudziwa zomwe zingachitike?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.41. Kodi Malamulo khumiwa amatiphunzitsa chiyani?

Y. Tikonde Mulungu komanso anthu ena.

Mayankho owonjezera:

1. Kodi umakonda abambo ako?
2. Kodi umadziwa kuwapangitsa abambo ako kuti akwiye? (Posawamvera kapena kumenyana ndi abale anga komanso anthu ena)
3. Kodi umawaonetsa bwanji abambo ako kuti umawakonda? (Powamvera komanso kukonda abale anga. Mwana atha kuyankha kuti '' powakumbatira'' koma nthandizeni kudziwa kuti abambo sadzamukumbatira ngati ali wosokoneza kapena wosamvera)
4. Kodi mumaonetsa bwanji kuti mumakonda Mulungu? (Posunga Malamulo ake)
5. Kodi mumaonetsa bwanji kuti mumakonda anthu ena? (posunga malamulo ake a Mulungu)
6. Kodi pali Malamulo angati a Mulungu? (Khumi)
7. Kodi ukudziwa kuti ndi malamulo angati amene amatiphunzitsa mmene tingamukondere Mulungu?
   (Anayi)
   Kodi ukudziwa kuti ndi malamulo angati amene amatiphunzitsa za kukonda ena?
   (Asanu ndi limodzi (6)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.42. Kodi lamulo loyamba ndi liti?

Y.Usakhale nayo milungu ina koma ine Ndekha.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi uli ndi abambo angati? (Amodzi basi)
2. Kodi ungawauze abambo ako kuti sindikufuna kuti mukhale bambo wanga koma ndikufuna akuti akuti kuti akhale bamboo wanga? '' Ukuganiza kuti bambo ako angasangalale utawauza choncho?
3. Kodi pali Amulungu angati? (Alipo Mulungu mmodzi yekha)
4. Nanga bwanji mafano osema a miyala ndi mtengo? (Awa onse ndi abodza)
5. Kodi tipemphere kwa milungu yonama? Nanga tiimvere? (Ayi, siingatimvere ndipo ndi yakufa ndi yopanda mphamvu.)
6. Kodi ukuganiza kuti Mulungu angakhale wosangalala ngati tipemphera kwa milungu yonama?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.43. Lamulo lachiwiri ndi liti?

Y. Usadzipangire iwe wekha fano losema kapena chirichonse ndikuchilambila

Mayankho owonjezera:
(Lamulo lachiwirili likukamba kwambiri za kapembedzedwe, ndipo china chilichonse chomwe Mulungu sanakhadzikitse kuti chipembedzedwe ncholetsedwa. Koma pakadali pano, tiyeni tingoona za kuletsedwa kwa mafano osema)

1. Kodi mukudziwa kuti fano kapena chosema ndi chiyani? (muyenera kuonetsa chosema komanso chithunzi cha munthu)
2. Kodi ungapange chifanizo cha Mulungu? Kapena ungajambule chithunzi cha Mulungu? (Ngati mwanayo anaonetsedwapo zithunzi zomwe zimayerekeza Mulungu , atha kuyankha kuti 'eya'. Ngati zatero, konzani izi mwamsanga kuti asasochere mmaganizo)
3. Palibe amadziwa mmene Mulungu amaonekera. Mukudziwa chifukwa chake? Kodi mukudziwa kuti simungathe kumuona Mulungu kapenanso kujambula chithunzi chake? (Chifukwa ali ngati Mzimu ndipo alibe thupi ngati lathu)
4. Poti sitidziwa mmene Mulungu amaonekera, Nanga tingapange chifanizo chake?
5. Mulungu amakwiya ndi anthu amene amayesera kupanga zifanizo zake. Izi ndi zomwe Lamulo lachiwiri likutiuza. Kodi mukuyenera kujambula chithunzi cha Mulungu?
6. Kodi mukuganiza kuti mpingo ukuyenera kukhala ndi zosema kapena zithunzi za Ambuye wathu Yesu Khristu?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.44. Lamulo lachitatu ndi liti?

Y. Usatchule dzina la Mulungu wako pachabe.

Mafunso owonjezera:

(Dzina lakuti 'Mulungu'limatanthauza zonse zimene iye amadzipangitsira kuti adziwike, koma pano tiona za tanthauzo lake lapafupi)

1. Dzina la abambo ako ndani? Kodi ukudziwa kuti dzina limeneli ndi la Abambo ako?
2. Kodi abambo ako angasangalale utawauza kuti susangalala ndi dzina limeneli?
3. Kodi ukudziwa kuti mayina a Mulungu ndi ati? (Yehova, Yesu, Khristu ndi ena otere)
4. Kodi umadziwa kuti uli ndi dzina la Mulungu? Kodi ndiwe Mkhristu? (Mwana wanu adziwe kunena kuti 'eya') Monga Mkhristu, mumakhala ndi dzina la Ambuye Yesu Mkhristu.
5. Kodi ukuganiza kuti Ambuye Yesu Khristu angasangalale ngati makhalidwe ako ali ngati a munthu yemwe si mkhristu ngakhale muli ndi dzina lake?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.45. Kodi lamulo lachinayi ndi liti?

Y. Udzikumbukira tsiku la sabata ndikulisunga loyera.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi musabata muli masiku angati?
2. Kodi ndi tsiku liti lomwe liri la sabata kwa akhristu? (Lamulungu)
3. Kodi mukudziwa dzina lina la tsiku la sabata? (Tsiku la Mulungu)
4. Kodi ndi chifukwa chiyani tsiku la sabata limatchedwa tsiku la Mulungu? (chifukwa ndi tsiku limene mwini wake ndi Mulungu)
5. Kodi muyenera kuchita chiyani pa tsiku la sabata? Nanga ndi chiyani chomwe muyenera kusachita patsikuli?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.46. Kodi lamulo lachisanu ndi liti?

Y. Lemekeza atate ako ndi amayi ako.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi abambo ako ndani?
2. Lamulo lachisanu likukuphunzitsa kuti uyenera kulemekeza atate ako ndi amayi ako. Kodi ukudziwa tikati 'kulemekeza'? (Tikutanthauza kupereka ulemu, kukonda komanso kumvera)
3. Kodi umawalemekeza bwanji makolo ako? (Powakonda komanso kuwamvera)
4. Kodi abambo ako atakuuza kuti uchite chinachake , iwe nkutenga nthawi kuti uchichite,kumeneku ndikuwalemekeza?
5. Ngati amayi ako atakuitana ali kuchipinda chophikirako , iwe nkumanamizira ngati sunamve kuitanako, kumeneku ndikuwalemekeza?
6. Ungaganizireko zinthu zina zomwe ungachite kuti ulemekeze makolo ako?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.47. Kodi lamulo lachiasanu ndi chimodzi ndi liti?

Y. Usaphe.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi ungaphe nyerere? Chimachitikira ndi chiyani nyerereyo ukaipha?
2. Mulungu sakutiuza kuti tisaphe nyerere kapena mphemvu. Mulungu akutiuza kuti tisaphe munthu mnzathu. Kodi mukudziwa mau amene amanenedwa pofuna kufotokoza kuphana anthu okha okha? (Kupha)
3. Mulungu amatiphunzitsa kuti tisaphe.
4. Mulungu amatiphunzitsanso kuti tisamakangane kapena kumenyana wina ndi mzake. Kodi ndi lamulo liti lomwe timaliphwanya ngati timenyana ndi mchimwene kapena mchemwali wathu?
5. Kodi mukaona anyamata awiri akumenyana mtchalichi, muyenera kuwauza chiyani? (Usaphe)
6. Kodi ukamenyana ndi mzako, uyenera kupanga chiyani? (Kumupempha kuti akhululuke komanso kupempha Mulungu kuti andikhululukire)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.48. Kodi alamulo lachisanu ndi chiwiri ndi liti?

Y. Usachite chigololo.

Mafunso owonjezera:

1. Lamulo lachisanu ndi chiwiri litiphunzitsa kuti mwamuna ndi mkazi sangagone chipinda chimodzi pokhapokha atakwatirana.
2. Kodi abambo ndi mwamuna kapena mkazi? Nanga amayi ndi mwamuna kapena mkazi?
3. Kodi Abambo ndi Amayi amagona chipinda chimodzi? Chifukwa?(Chifukwa ndi okwatirana)
4. Lamulo lachisanu ndi chiwiri limtiphunzitsanso kuti tizivala bwinobwino. Ungandiuze mmene tiyenera kuvalira?

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.49. Kodi lamulo lachisanu ndi chitatu ndi liti?

Y. Usabe.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi ukudziwa tanthauzo la kuba? (Uku ndikutenga chinthu kuchokera kwa wina popanda chilolezo)
2. Kodi munthu amene amaba zinthu timamutchula kuti ndani? (Wakuba kapena Mbava)
3. Kodi utaona botolo loti muli switi liri muchipinda china cha tchalichi, ungatengeko switi popanda chilolezo? Nanga ndi lamulo liti limene ungaphwanye ngati utachita zimenezi?
4. Kodi ndibwino kuti utsegule momwe mchimwene wako anasungamo zoseweretsa zake nkutenga kukaseweretsa popanda kumupempha? (Pamene mwana alibe mchimwene wake, tchulani m'bale aliyense kuti zigwirizane)
5. Kodi ukatenga chinthu popanda chilolezo,uyenera kuchita chiyani? (ndiyenera kuchibweza kenaka nkupempha Mulungu kuti andikhululukire)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.50. Kodi lamulo lachisanu ndi chinayi ndi liti?

Y. Usamnamizire mnzako.

Mafunso owonjezera.

1. Kodi ukudziwa tanthauzo lakumnamizira wina? (Kunena bodza)
2. Kodi munthu wonena bodza timamutchula kuti ndani? (Wabodza)
3. Kodi utamenyana ndi m'bale wako ,iwe nkukhala woyambitsa kumenya, ungauze Abambo ako kuti wayambitsa ndi winayo? Kodi utanena choncho, ukhala kuti ukuchita chiyani?
4. Kodi utajambula pakhoma ndiye Amayi nkufunsa amene wachita izi, Uyenera kunenakuti chiyani? Ngati Amayi adzakukwapula chifukwa chojambula pakhoma, unganene kuti sunajambule ndiwe?
5. Kodi ukanena bodza, uyenera kuchita chiyani? (Ndinene zoona ndikuuza Mulungu kuti andikhululukire tchimo langa)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.51. Kodi lamulo lachikhumi ndi liti?

Y. Usasilire.

Mafunso owonjezera:

1. Kodi mukudziwa tanthauzo la kusilira? (Uku ndi kufuna kukhala ndi chinachake kwambiri moti nthawi zonse umangochiganizira)
2. Kodi ngati ukufuna switi, Amayi nkunena kuti ayi, Uchite chiyani?
3. Kodi ukudziwa lamulo lomwe ungakhale ukuphwanya ngati ulumphalumpha ndi kulira chifukwa Amayi anena kuti ayi pamene ukufuna switi?
4. Ngati upitiliza kupempha Amayi kuti akugulire choseweretsa chomwe mnzako ali nacho,ukudziwa lamulo lomwe ukuphwanya?
5. Ngati usilira chinachake, uchite chiyani (Ndipemphe Mulungu kuti andikhululukire tchimo langa)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

F.52. Kodi pemphero nchiyani?

Y. Kuyankhula ndi Mulungu.

Mafunso owonjezera.

1. Kodi ungamuone Mulungu? (Ayi, koma Iye amandiona)
2. Kodi ungamumve Mulungu? (Ayi, koma ndimamva mau ake omwe amalalikidwa)
3. Kodi ukuganiza kuti Mulingu angakumve? (Inde, monga momwe amandimvera)
4. Mulungu amakukonda. Ukuganiza kuti angakondwe kukumva iwe ukuyankhula naye?
5. Ungaphunzire kudziwa mmene ungayankhulire ndi Mulungu pomvera Amayi komanso Abambo akamapemphera. Kodi ungafune kuyankhula ndi Mulungu?

Copyright © Gratia Dei Sola Media